Baibulo ya ana
Ikupasilani

Paneme Mulungu anapanga zonse





Yolembedwa ndi: Edward Hughes
Yojambulidwa ndi: Byron Unger; Lazarus Alastair Paterson
Yotengedwa ndi: Bob Davies; Tammy S.
Yotathauzidwa ndi: Phiri Williams
Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

BFC
PO Box 3
Winnipeg, MB R3C 2G1
Canada

©2020 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Anatipanga ife ndindani? Baibulo, mau a Mulungu amanena zamomwe munthu analengedwela ndi chiyambi cha munthu. Kalekale, Mulungu analenga munthu woyamba ndikumutcha dzina loti Adamu.



Mulungu analenga Adamu kuchokera ku mfumbi la dziko la pansi. Pamene Mulungu ana mpumira mwa Adamu, anakhala wa moyo. Anapezeka yekha mmunda wokongola wotchedwa kuti Edeni.



Pamene Mulungu asadalenge Adamu, iye anapanga dziko ndi zinthu zokongola. Pan'gono ndi pan'gono Mulungu anapanga malo okwera, maluwa onunkhira ndi mitengo yayitali, mbalame za mapiko wowala ndi njuchi ndi nkhono zo telera.

Pachiyambi penipeni, Mulungu asadalenge zonse, panalibe chilichonse kupatula Mulungu yekha. Kunalibe anthu kapena malo kapena zinthu. Panalibe. Panalibe kuwala kapena mdima, panalibe kukwera kapena kutsika. Kapena mawa kapena dzulo. Kunali Mulungu yekha amene alibe chiyambi. Kenaka Mulungu anachita! Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi.



Ndipo dziko linalibe maonekedwe alionse. Ndipo mdima unali pamwamba pakuya. Kenaka Mulungu anati. "Pakhale kuyela."



Ndipo kunayeradi. Mulungu anatcha kuyera kukhala usana ndipo mdima kukhala usiku. Ndipo panali madzulo ndi m'mawa tsiku loyamba.



Tsiku la chiwiri, Mulungu adasonkanitsa madzi pamodzi. Patsiku lachitatu, Mulungu adati, "pakhale mtunda." Ndipo zinachitikadi.



Mulungu adalamula udzu ndi maluwa ndi mitengo kumera pa dziko. Ndipo zinachitika. Ndipo panali madzulo ndi mmawa tsiku la chitatu.



Ndipo Mulungu analenga dzuwa,
ndi mwezi, ndi nyenyezi zambiri
zoti palibe anakaziwerenga.
Ndipo madzulo ndi mmawa
ndiro tsiku lachinayi.



Zolengedwa za mnyanja ndi somba ndi mbalame ndizo mwa zina Mulungu anaikapo. Tsiku la chisanu Mulungu ndipo adalenga zinsomba zazikulu ndi zoyenda yenda zamoyo zochuluka m'madzi. Mulungu analenga mtundu uliwonse wa nsomba kuti zikakwanire dziko lapansi ndiponso mitundu ya mbalame pa dziko ndi mnyanja ndi mlengalenga. Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku la chinai.

Ndipo patatha izi, Mulungu analankhulanso. Ndipo anati, "Dziko libweretse zolengedwa zamoyo ..." Ndi nyama zonse ndi zombe ndi abuluzi anakhala ndi moyo. Panalinso njomvu zogwedeza komanso anyani ndi n'gona.

Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa wa lachisanu.



Mulungu anapanga chinthu china tsiku lachisanu ndi chimodzi mwapaderadera. Zonse zinali zitakonzeka kwa munthu. Panali chakudya ndipo panali nyama kumutumikira iye. Ndipo Mulungu anati, "Tipange munthu mchifaniziro chatu ndi mchikhalidwe chathu kuti alamulire padziko lapansi".



NDIPO MULUNGU ANAPANGA MUNTHU MUCHIFANIZIRO CHAKE; NDI MCHIFANIZIRO CHAKE ANAPANGA MUNTHU.

Mulungu
analankhula
ndi Adamu.
“Idya chimene
ufuna kuchokera
mmundamu. Koma
usadye chochokera
mumtengo wodziwitsa
zabwino ndi zoipa.
Ngati uzadya kuchokera
pamtengowo zedi
uzafa ndithu.”



Ndipo Mulungu anati, "sikwabwino kuti munthu akhale yekha. Ndidzampangira womthangatira iye."

Mulungu anabweretsa mbalame ndi zilombo kwa Adamu. Adamu anazitcha maina zonse. Mulungu anali wochenjera pakupanga izo. Komano panalibe weniweni mnzake wa Adamu.

Mulungu anapatsa tulo tofanato Adamu, ndikuchosa nthiti yake imodzi. Ndipo Mulungu anapanga mkazi kuchkela ku nthiti. Mkazi ameneyo Mulungu anampanga anakhala oyera kwa Adamu.



Mulungu anapanga zonse m'masiku asanu ndi limodzi. Ndipo Mulungu anadalitsa tsiku la chisanu ndi chiwiri ndi kukhala lopumula. M'munda mwa yedeni Adam ndi Eva mkazi wake anakhala ndi chisangalaro chomvera Mulungu. Mulungu anali Mbuye wawo, wobweretsa zosowa zawo.

Paneme Mulungu anapanga zonse

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

Genesis 1-2

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16